


**Kapangidwe ka fetereza
wochokera ku zomera**

**Pogwiritsantchito tizilombo
ta munthaka**



Buku 1

Zam'katimu

Kufotokoza za fetereza wochokera ku zomera 1




Kapangidwe ka fetereza wochokera ku zomera 4

Kupanga fetereza kuchokera ku zinyalala 6




Kupanga fetereza 10

Kugwiritsa ntchito fetereza wolimba



Kugwiritsa ntchito fetereza wopangidwa ku zomera 18






Kufotokoza za fetereza wochokera ku zomera

Kuperekha chonde ku dothi

Dothi la chonde ndi chinthu chofunikira kwambiri pa ulimi chifukwa choti zomera, nyama ndi anthu amadalira dothi. Kuonjezera chonde mu dothi kumachititsa mbeu ndi zifuyo zathu kukhala zathanzi. Mbeu ndi zifuyozи sizigwidwa kwambiri ndi tizilombo komanso matenda izi zimachititsa kuti zipitirire kukhala zathanzi ndi zopindulitsa.



Pofuna kusamalira dothi, tiyenera kumvetsetsa kuti dothi linapangidwa ndi zinthu za moyo ndi zopanda moyo. Zinthu zopanda moyo zimapangidwa kuchokera ku miyala yomwe yasweka, tizilombo tokufa komanso zomera zomwe zawola (monga masamba amene agwa ndipo ayamba kuwola). Zamoyo zomwe zimaonjezera chonde mu nthaka ndi tizilombo ting'oning'ono tomwe timakhala mu dothi. Tina ta tizilomboti (monga chiswe, nyongolotsi ndi tizilombo touluka) ntatikulu moti timaoneka ndi maso koma tambiri sitingaoneke ndi maso athuwa pokhapokha tigwiritsi ntchito chipangizo chomwe chimakuza tizinthu ting'ono-ting'ono. Tizilombo totere muli mamiliyon i a mabakiteriya ndi mafangayi.



Tizilombo ta mu nthaka komanso chonde

Tizilombo ta mu nthaka ndi tofunikira kwambiri popititsa patsogolo chonde mu nthaka. Tizilomboti timatenga tizinthu topanda moyo tokhala mu dothi ndi kutipanga kukhala chakudya cha zomera.

Fetereza wopangidwa ndi makemiko, pambali poti ndi wokwera mtengo komanso amasowa, feterezayu amaphanso tizilombo ta mu nthaka. Ichi ndi chifukwa chimodzi chimene fetereza wa makemikoyu amachevertscha chonde mu nthaka akagwiritsidwa ntchito.

Njira yapafupi ndi yosaboola mthumba pofuna kuonjezera chonde mu nthaka ndiyo kulimbikitsa kuti pakhale tizilombo ta mu nthaka topindulitsa tochuluka ndi kutipatsa malo abwino kuti tichulukane. Tizilombo totere timadya tizinthu ta mu dothi, timachulukitsa chonde ndipo timachititsa zomera kupeza chakudya nthawi zonse. Feterezayu amapangitsa kuti tizilombo ta mu nthaka tichulukane ndi kupeza chakudya.




Kodi fetereza wochokera ku zomera n'chiyani?

Fetereza wochokera ku zomera ndi kasakaniza amene mkatи mwake muli tizilombo ta mu nthaka topindulitsa. Tizilombo timenetи timakulitsa zomera pochulukitsa chonde ku zomera ndi kulimbikitsa kakulidwe ka mizu ya zomera. Fetereza wina wochokera ku zomera amakhala wolimba mwachitsanzo wa bokashi (feterezayu wafotokozedwa mu buku lina). Pomwe fetereza wina ndi wa madzi. Fetereza wina monga wa bokashi amapangidwa pamalo pomwe pakudutsa mpweya pomwe fetereza wina safuna mpweya, monga fetereza wochokera ku zomera koma wamadzi amene wafotokozedwa m'mabuku ena.

N'chifukwa ninji tiyenera kupanga fetereza wochokera ku zomera?

Fetereza wochokera ku zomera ali ndi phindu lochuluka. Akhoza kupangidwa pogwiritsa ntchito zipangizo zopezeka mosavuta, amachulukitsa chonde mu nthaka, komanso amakhala ndi chonde kwa,biri kuposa manyowa opangidwa ku ndowe.

Fetereza opangidwa ku zomerayu savuta kupanga kusiyana ndi wa ndowe ndipo akhoza kugwiritsidwa ntchito pofuna kukonza ndi kubwezeretsa chonde pa malo akulu kusiyana nkuti eni malowo akanangodalira fetereza wopangidwa ku ndowe komanso manyowa wamba. Fetereza wopangidwa ku zomera koma ali wamadzi akhoza kusungidwa kwa chaka chimodzi kapena kuitirira apo popanda kutha mphamvu kapena kuulukamo. Fetereza wotereyu amachititsango zomera kuirira ku tizilombo ndi matenda.




Kapangidwe ka fetereza wochokera ku zinalala

Mitundu yambiri ya fetereza wochokera ku zomera imapangidwa pogwiritsa ntchito njira imene imatchedwa. Kusasitsa kotere ndiko kusintha kwa chinthu chifukwa cha zimene tizilombo tachita. Mwachitsanzo, mbeu monga mawere ndi chimanga zikhoza kufunditsidwa kuti zimere ndipo patsogolo zipangidwe mahewu kapena mowa pogwiritsa ntchito mamaikilobu otchedwa isiti. Isiti amadya shuga amene ali mu mawere ndi chimanga chija kenako amasintha zinthuzo kukhala mahewu kapena mowa (ngati zasiidwa kwa masiku angapo). Mkaka umathanso kusawa chifukwa cha mabakiteriya okhala ndi asidi omwe amatchedwa lactic.

Popanga fetereza wochokera ku zomera timaonetsetsa kuti tikuperekta malo abwino oti tizilombo ta mu nthaka tichulukane komanso kudyetsa ito chakudya chomwe ito timakonda kudya. Izi zimachititsa kuti pabwera tizilombo tosiyanasiyana tomwe timaperekta chakudya ku zomera ndi kuchulukitsa chonde mu dothi.

Kupeza ndi kuchulukitsa tizilombo ta mu nthaka


Tizilombo ta mu nthaka tikhoza kutengedwa kuchokera ku malo achilengedwe monga nkhalango kapena kupangidwa pogwiritsa ntchito masamba omwe aikidwa mu dothi.



Kupeza tizilombo ta mu nthaka topezeka ku dera komweko

Malo abwino kwambiri komwe kungapezeke tizilombo ta mu nthaka ndi mu nkhalango. Nthawi ya dzinja ndiye yabwino kupeza ndi kutenga tizilomboti chifukwa choti timakhala tikutakataka. Pezani nkhalango yowirira bwino. Mupite pa malo amene masamba ogwa mu mtengo aunjikana mochuluka. Sefani masambawo pogwiritsa ntchito manja, ndipo mutenje masamba a pansi omwe ayamba kuwola, awa akhale masamba amene mukuona kuti akumera tinguwi toyera. Tinguwi timeneti timapangidwa kuchokera ku masamba omwe avunda pamwamba pa dothi.

Tinguwi timeneti timatchedwa zivundira ndipo timakhala ndi tizilombo ta mu nthaka tochuluka. Tengani mlingo wa masamba omwe mukufuna ndipo masamba osavunda omwe anali pamwamba aja muwasiye pomwepo. Muonetsetse kuti musaononge nkhalango. Ngati simungathe kupeza masamba ovunda kapena muli mu nthawi ya chilimwe ndiyetu mukhoza kupanga nokha.




Sefani masamba, ndi kutenga a pansi owola.

Kupanga manyowa kuchokera ku masamba zofunikira


- Ndowa imodzi ya ufa wa makala opangidwa kuchokera ku zinyalala.
- Ndowa imodzi ya ufa wa makala opangidwa kuchokera ku zinyalala.
- Matumba awiri kapena atatu a deya. Amenewa ngokwanira (amagwiritsidwa ntchito pongowaza mu manyowawo). Deya ndi zotsalira mukamakonola mbeu. Amagwiritsidwa ntchito podyetsera zifuyo. Mukhoza kugwirtsa ntchito madeya ochokera ku mpunga, tirigu kapena chimanga.
- Mamolasi kapena shuga (mamolasi okwana theka la lita, kapena magalamu 500 a shuga wosungunulidwa m'madzi; mulingo si wofunikira kwambiri-bola madzi a shuga basi).

Kapangidwe ka makala kuchokera ku zinyalala


1. Muike nthambi za mitengo ndi mphukira zomera pa nthambi za mitengo mu dzenje losaya. Iyi ndi njira yabwino yochotsera nthambi zosafunika zomwe zili ndi minga.
2. Tenthani nthambizo/mphukirazo kufikira utsi uchulukane kenako mufotsere ndi dothi losapitirira masentimita awiri mulitali.
3. Lolani nthambi/mphukirazo zinyeke kufikira zitada
4. Zimitsani motowo ndipo mutenge makala omwealipowo.



Kapangidwe kake



1. Kumbani dzenje loya 20 sentimita ndipo mmbali likhale mukhale 40 sentimita.
2. Muike pansi pa dzenjelo ufa wa makala uja.
3. Kenako muike masamba ouma, asatalike kupita m'mwamba kuposera masentimita 10, kenako muwazepo madeya pang'ono.






4. Sakanizani mamolasi kapena shuga uja m'madzi okwana malita 20 ndipo muwaze m'dzenje lija ndipo muwaze makapu teni a madziwo m'dzenjemo.



5. Pitirizani kuika ufa wa makala uja pamodzi ndi masamba komanso mamolasi kapena shuga uja pa mlingo womwe wanenedwa pamwambawo kufikira mutapanga mulu waukulu m'dzenjemo.
6. Vundikirani dzenjelo ndi chisaka chakale kuti chithandizire kusunga chinyezi m'dzenjemo.



7. Kasakanizayu akhale ndi chinyezi koma asanyoweretu. Dikirani kwapafupifupi mwezi umodzi kenako mukhoza kudzagwiritsa ntchito manyowawa popangira fetereza wopangidwa kuchokera ku tizilombo ta mu nthaka (zafotokozedwa tsamba lotsatira).



Kupanga fetereza wolimba kuchokera ku zinyalala

Njira imeneyi idzakuthandizani kuchulukitsa tizilombo ta mu nthaka timene munatitenga ku nkhalango kuti mupangire fetereza wolimba amene angagwiritsidwe mu njira zambiri zopindulitsa.


Zinpangizo

- Ndowa imodzi ya malita 20 yokhala ndi chivundikiro
- Makilogalamu anayi a zinyalala zovunda kapena masamba ovunda
- Makilogalamu 8 a deya
- Malita awiri a mamolasi kapena magalamu 750 a shuga amene wasungunulidwa ndi madzi
- Madzi (pa mlingo uliwonse ungafunikire)

Ngati mugwiritsa ntchito mgolo wa malita 60, ndiye kuti muyenera kuchulukitsa zipangizo katatu. Ngati madzi ali malita 200 ndiye kuti zipangizo zichulukitsidwe ka khumi.

Kapangidwe kake

Sakanizani bwino lomwe zinthu zatchulidwa pamwambazo.
Samalani, musathire madzi ambiri.



Kuti mudziwe kuti madzi akwana yesani kukowa pang'ono zomwe mwasakanizazo ndipo mukulunge chinthu chonga 'soseji.' Mukachifinya chinthucho kwambiri, ndipo sichikutulutsa madzi pa zala zanu ndiye kuti madzi alimo okwana.

Ikani zinthu zomwe mwasakaniza zija (zitalike masentimita 15) mu ndowa kapena mgolo ndipo musinje ndi musi kuti zipite pansi.

Ngati mukugwiritsa ntchito mgolo wa malita 60 kapena 200 ndiye nzotheka munthu kukwerapo nkumaponda kuti zisakanikirane bwino.



Ikaninso kasakaniza wina wotalika masentimita 15 ndipo musinjenso monga mudachitira ndi zoyamba zija. Cholina ndi choti mpweya uchoke. Njirayi njofuna kuti zinthuzi ziwole ndi kuchulukitsa tizilombo ta mu nthaka popanda kugwiritsa ntchito mpweya.

Ikaninso kasakaniza wina wotalika masentimita 15 ndipo musinjenso monga mudachitira ndi zina zija kufikira mgolowo utsale pang'ono kudzaza. Mgolovo usadzaziretu, kukamwa kwake musiye malo okwana masentimita 10 kapena 15. Vundikirani kuti mpweya usalowe. Zisiyeni zinthuzo zikhale kwa masiku 30.


Kugwiritsa ntchito kasakaniza wolimba wopangidwa ndi tizilombo ta mu nthaka

Kasakaniza wolimba wopangidwa ndi tizilombo ta mu nthaka amagwiritsidwa ntchito mu zinthu zambiri. Ntchito ina ndiyo kuthandizira kuchulukitsa tizilombo mu nthaka. Mukafuna kutere mukhoza kutsata njira inaperekedwa ija koma mmalo motenga zipangizo za ku nkhalango mukhoza kugwiritsa ntchito makilogalamu anayi a kasakaniza wolimba wa tizilombo ta mu nthaka mu kasakaniza wina mukufuna kupangayu, muziike mu mgolo ndi kuzisiya zikhale kwa masiku 30.

Ntchito zina za kasakaniza wa mamaikilobu ndi monga: kudyetsera zifuyo kuti zitetezeke ku matenda, ntchito ina ndiyo

kuchulukitsa chonde mu fetereza wina wachilengedwe ndi manyowa opangidwa ku ndowe, ntchito inanso ndi kuvunditsa zinthu zochokera ku malo ophikira, komanso kupangira mankhwala othira mu mbeu.

Chikhaliirecho ntchito ina ndiyo kupangira fetereza wachilengedwe wa madzi, zambiri tikamba tsamba lotsatira.




Kupanga fetereza wamadzi kuchokera ku zomera

Fetereza wotere amapangidwa mu njira ziwiri. Poyamba, isiti ndi timabakiteriya timasinthia zinthu zopangira feterezayu kupyolera mu kuzivunditsa. Chotsatira, ma bakiteriya a asidi wa lacticamasintha manyowa aja kukhala ndi asidi. Njira ziwigizi zimachititsa kuti manyowawo atulutse zinthu zofunikira, kuphatikizapo chakudya cha dothi ndi michere imene imachititsa dothi kukhala ndi chonde komanso mbeu zimakula bwino.

Zipangizo

- Bigiri Kachinthu kolumikizira paipi ndi bigiri
- Nipo
- Paipi
- Ndi botolo lapulasitiki



Njira imeneyi siifunika kuti mpweya ulowe mu bigirimo mwa ichi mudzayenera kukhala ndi kontena imene ingatsekeke mwakuti mpweya usalowe. Migolo ya malita 200 ndi malita 60 imene ili ndi kam'bowo kokhala ndi kotsekera kachitsulo imagwira ntchito bwino. Mukhozanzo kugwiritsa ntchito bigiri imene ili ndi chotsekera chimene sichilora mpweya kulowa.

Muonetsetse kuti mpweya uzituluka osati kulowa mu bigiri kapena mu mgolo wanuwo. Chitsanzo chili mu chithunzi chili pa tsamba lotsatira.

Muboole pamwamba pa bigiri kuti muthe kuika ka chinthu kolumikizira paipi ndi bigiri kaja komanso nipo. Pamene pa mulumikizepo paipi imene muyiyikenso m'mbotolo la madzi. Botololi likhoza kukhala pa mbali pa bigiri yanu.



Mangani paipi bwino bwino ndipo musalole mpweya kulowa, koma gasi wochokera mu bigiri ndiye ayenera kudutsa mu papipi yanuyo. M'dziko la Kenya alimi asankha kuvundikira bigiri yawo ndi chipulasiti komanso chubu chakale cha njinga.

Mu bigiriyi gasi amakhala akuchulukana mwa ichi ayenera kutulutsidwa nthawi ndi nthawi.




Zipangizo zina



Ndondomeko yafotokozedwa pamwambapo ndi ya bigiri ya malita 60. Koma ngati mukugwiritsa ntchito mgolo wa malita 200, ndiye kuti muchulukitse katatu zipangizo zafotokozedwa pamwambapo. Ngati mukugwiritsa ntchito bigiri ya malita 20 (monga zaonetsedwa mu chithunzi pamwambapo) gwiritsani ntchito gawo limodzi la magawo atatu la zipangizo zafotokozedwazo.

- Kasakaniza wolimba wa tizilombo ta mu nthaka: makilogalamu anayi (gwiritsani ntchito ndondomeko imene yafotokozedwa m'kabuku kano).
- Mamolasi: malita anayi kapena makilogalamu awiri a shuga wosungunulidwa m'madzi. Mamolasi ndiwo abwino kwambiri koma zikavuta gwiritsani ntchito shuga wosungunulidwa m'madzi.
- Mkaka kapena zotsalira zake: ukhale malita awiri kapena anayi. Wabwino kwambiri ndi mkaka wosathira madzi umene wakamidwa ku ng'ombe. Mkakawo ugone tsiku limodzi kenako tsiku lotsatira mudzachotse chinthu chomwe chayalana pamwamba pakepo. Inu mudzagwiritsa ntchito mkakawo. Mukhozanso kugwiritsa ntchito mkaka umene mwagula ku sitolo. Mkaka umene uli ndi mafuta ochepa ndiwo wabwino. Zikavuta gwiritsani ntchito zotsalira za mkaka-izi ndi zija zimatsalira mukasefa mkaka wosawa. Ngati mugwiritsa ntchito zotsalira za mkakazi ndiye akhale malita asanu ndi limodzi.
- Makilogalamu awiri a phulusa, fumbi la miyala kapena ufa wa mafupa operedwa bwino apo ayi mukhozanso kugwiritsa ntchito ziwiri zonzezi.
- Madzi: gwiritsani ntchito madzi a ku chitsime kapena a pa mjigo osati a pa mpopi chifukwa choti a pa mpopi amakhala ndi mankhwala a kololini.




Ndondomeko yake

Ikani makilogalamu anayi a kasakaniza wa tizilombo ta mu nthaka uja mu mgolo wa malita 60. Mu chitini china, sakanzani mkaka, mamolasi, phulusa, fumbi la miyala ndi ufa wa mafupa uja pogwiritsa ntchito madzi. Thirani zimenezi mu mgolo muja muli zinthu zina zija, ndipo takasani bwino lomwe. Dzadzani mgolowo ndi madzi, mungosiya mpata wa masentimita 10. Vundikirani mgolowo bwino lomwe mwakuti musalowe mpweya ndipo tulutsani paipi yomwe ikulowa mu botolo la madzi (onani chithunzi chomwe chili pa tsamba 14).

Zisiyeni kwa kwa masiku ndithu kuti zisakanikirane bwino lomwe kufikira pamene thovu laleka kuoneka. Izi zikhoza kutenga masiku 30. Musagwiritse ntchito feterezayu asanakwane masiku 30

kuchokera pa tsiku lomwe mwamupanga, ngakhale thovu litasiya kuoneka.

Onetsetsani kuti zinthuzi zikuoneka ndi mtundu ngati wa fanta kapena wa khofi ndipo zisanunkhe mosowetsa mtendere. Zizinunkhira ngati mowa wopangidwa mwachilokolo. Ngati zikununkha mosowetsa mtendere ndiye mutaye. Ngati zikununkhira ndiye kuti zidzagwira bwino ntchito ndi kuthandiza mbeu.






Kasungwidwe ka feterezayu

Ikani feterezayu mu botolo kapena mu chigubu chomwe chavundikiridwa bwino lomwe. Vundikirani pamene mwatengamo fetereza wina amene mwathira kapena mukufuna kuthira mu mbeu zanu. Feterezayu akhoza kukhala kwa nthawi yaitali. Ngati fungo lake lili losanunkha mukatsekula kuti mutenge fetereza wina woti mugwiritse ntchito, ndiye kuti feterezayo ali bwino bwino sanaonongeke. Ikani malo abwino pomwe sipakuombedwa ndi dzuwa.

N'kwabwino kumaonjezera mamolasi okwana 100ml nthawi iliyonse mwatsekula fetereza wanu kuti tizilombo tizipeza chakudya! Apo ayi, pamene mukupanga feterezayu ndipo mwamaliza kuthira mamolasi kapena shuga, sefani ndipo madzi akewo muiike m'mabotolo kapena mu zigubu koma akhale oti zikhoza kutsekedwa.





Kagwiritsidwe ntchito ka fetereza wochokera ku zomera

Tengani fetereza wa madziyu wokwana lita imodzi ndi kusungunula ndi malita 20 a madzi nkuthira mbeu zanu. Zikutanthauza kuti ngati sipuleya yanu ndi ya malita 20, ndiyе kuti muikemo fetereza wokwana lita imodzi kwinako muonjezere madzi. Poperani feterezayu kunsi kwa masamaba a mbeu zanu, kaya ndi ndiwo za masamba, mitengo kapena mbeu zina.

Poperani feterezayu m'mawa kapena chakumadzulo. Nthawiyi mpamene masamba a mbeu amatsekula timabowo tawo. Palibe mulingo wokhazikika wa nthawi ya kathiridwe. Koma anthu ambiri amapopera kamodzi pa mlungu kapena kamodzi pa milungu iwiri ilyonse.



Feterezayu amapereka chakudya ku mbeu kuti zikule bwino (michere, mavitamini, asidi, ndi michere ina). Feterezayu amadyetseranso tizilombo tomwe timakhala pa masamba a mbeu ndi m'dothi.

Feterezayu amakopanso tizilimbo tochuluka kuti tibwere mu dothi lomwe lazungulira mbeu. Mwa ichi, feterezayu ndi wopindulitsa ku mbeu komanso ku dothi.



Photo credit: Markus Lemke




Photo credit: Markus Lemke

Chithunzi 1: Alimi ang'ono ang'ono kwa Chintumbira, Blantyre momwe akuphunzira kukonza fetereza wa mbeya komanso fetereza wa chirengedwe (March 2025).

Chithunzi 2: Alimi ang'ono ang'ono kwa Mtema, Nsanje momwe akuphunzira kukonza fetereza wa chirengedwe (June 2023).

BIOFERTILIZER

KAPANGIDWE KA FETEREZA WAMPHAMVU WA CHIRENGEDWE



KAPANGIDWE KA FETEREZAYU



1. Thirani madzi a mlingo wa malita 100 mu mgolo wa malita 200. Kenako thirani ndowe zokwana 40Kgs ndi kutakasa (ndowe za Mbuzi ziyanera kuyikidwa m'madzi ndi kuzisinja). Thiraninso 5-10kgs ya manyowa a kompositi ndi 4 kgs ya Makala osinja bwino.
2. Onjezerani 2kgs ya masamba awisi osinja ndi kutakasa.
3. Sungunulani malita 4 a Mkaka ndi malita 4 ama Molasezi mu madzi okwana malita 10. Kenako thirani zonsezi mumgolo muja ndikuzitakasa bwino.
4. Sungunulani zipangizo zotsala zonse mu madzi amalita 10 ndi kutakasa mokwanira bwino.
5. Dzadzani mgolo ndi madzi mpaka pa mlingo wa malita 180.
6. Tsekerani bwino chotsekera kuti musamalowe mpweya uliwonse.. Kenako boolani kabowo pa chotsekera chija ndikuikapo paipi yomwe mbali ina iyikidwe mu botolo la madzi lomangiridwa pa mgolo uja. Izi zimathandiza kuti mpweya udzitha kutuluka koma wakurja usamalowemo.
7. Sungani mgolo wa fetereza pamalo otchingika bwino osafika dzuwa ndi mvula. Kutenthera kwabwino kwamalo osungirawo kukhale pakati pa 38°C ndi 40°C.
8. Dikirani kwa masiku osachepera 30 mpaka 35 kuti mutsegule ndikuona mmne fetereza alili poona kaonekedwe ka ntundu ndi fungo lake.

Chenjezo: Ngati pamwamba pa fetereza pakuoneka zinthu zooneka zoyerwa kapena akumveka fungo losiyana ndi manyowa kapena ndowe zaziwisi, fetereza ameneyo asagwiritsidwe ntchito chifukwa cha tizilombo tina toononga timene tingapezeke. Izi zimachitika nthawi zambiri ngati chotsekera sichinatsekeke bwinobwino.

Buku lino likupereka uthenga wokhudza fetereza wopangidwa kuchokera ku zinalala. Likuperekanso njira zosavuta zowathandiza alimi kupanga fetereza wotere pa minda yawo pogwiritsa ntchito zipangizo zosavuta kupeza.

Kuti mudziwe zambiri zokhudza njira izi zopangira fetereza wochokera ku zinalala mukhoza kupita pa webusayiti yathu iyi www.seedandknowledge.org.



Bukuli lasindikizidwa ndi chithandizo chochokera ku Brot fur die Welt komanso the Swiss Agency for Development and Cooperation (SDC).

Bukuli lidamasuliridwa ndi Sidreck Chingwalu ndi thandizo komanso upangiri ochokera ku Churches Action in Relief and Development (CARD).



Bread for the World -
Protestant
Development Service



Schweizerische Eidgenossenschaft
Confédération suisse
Confederazione Svizzera
Confederaziun svizra

Swiss Agency for Development
and Cooperation SDC